Baibulo ya ana
Ikupasilani



Elisa,
Munthu
Wozizwitsa

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Lazarus
Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: Ruth Klassen

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Panalibe ng'ombe zokwanira kukokera khasu.

Panafunikanso chimodzi. Zimenezo sizinalepheretse mlimi wachinyamata wotchedwa Elisa! Anangodziphatika ndi ng'ombe zija, n'kutenga malo osowa. Ayenera kuti anali munthu wamphamvu, Wanzeru komanso

Wolimbikira ntchito.

Pamene Elisa anali kulima,
Eliya mneneri wa Mulungu
anafika pafupi ndi kumuitana.
Mnyamatayo anasiya munda
wake kuti akakhale mtumiki
wa Mulungu. Tsiku lina,
Mulungu anatenga Eliya
kupita kumwamba ndi
kamvuluvulu.
Tsopano Elisa
anali mneneri
wa Mulungu kwa
Israyeli.

Ngakhale kuti Elisa
anali ndi chisoni
chifukwa chakuti
Eliya anali
atachoka,
iye anapemphera
kuti Mulungu
amupatse mphamvu
ngati ya Eliya.

Elisa anatenga chovala cha Eliya n'kumenya madzi oyenda mumtsinjewo ngati mmene Eliya anachitira. Madzi anagawanika!
Tsopano Elisa anadziwa kuti Mulungu anali naye.

Pamene Elisa anali kupita ku mudzi wina

wotchedwa Beteli, achichepere ena anam'nyoza kuti, "Kwera wadazi iwe!" Iwo sanasamale kuti Elisa anali mtumiki wa Mulungu. Chinthu chodabwitsa chinawachitikira. Zimbalangondo ziwiri zazikazi zinatuluka m'nkhalango n'kukaphwanya ana aamuna makuni anayi ndi awiri 42.

Tsiku lina Elisa anakumana ndi mkazi wamasiye amene anali ndi ngongole imene sanathe kubweza.

Kuti atenge ndalama zake, wobwereketsayo ankafuna kutenga ana aamuna awiri a mkazi wamasiyeyo kuti akhale akapolo. "Pita ukabwereke zotengera kwa anansi ako onse... zotengera zopanda kanthu," anatero Elisa. Mulungu akanati amuchitire chinthu chodabwitsa mayi ameneyo.

Mkazi wamasiyeyo anali ndi botolo la mafuta m'nyumbamo. Koma mumtsuko waung'onowo anathira mafuta okwanira kudzaza ziwiya zonsezo! Ngati iwo anali ndi mabafa m'masiku amenewo, kodi mukuganiza kuti Mulungu akanadzaza nawonso? Mkazi wamasiyeyo anagulitsa mafutawo napulumutsa ana ake aamuna.

Mayi wina ndi mwamuna wake anamanga chipinda chapadera m'nyumba mwawo kuti Elisa azikhalamo akamadutsa. M'chipindamo anaika bedi, tebulo, mpando, ndi choikapo nyale. Chipinda chimenecho nthawi zonse chinali cha Elisa.

Elisa anadabwa kuti abweza bwanji kukoma mtima kwa banjali. Atadziwa kuti alibe ana, ananena zinthu zimene mayiyo sanakhulupirire. "Chaka chamawa nthawi ngati ngati ino, udzakumbatira mwana wamwamuna." Ndithudi, patapita chaka, mwanayo anabadwa.

Patapita zaka zingapo mwana yemweyo anali kumunda ndi bambo ake. “Mutu wanga, mutu wanga,” mnyamatayo analira. Pamene anadza naye mwanayo kwa amake, iye anakhala pa maondo ace mpaka usana, namwalira. Mayiyo anagoneka mwanayo pakama m’chipinda cha Elisa.

Mukuganiza kuti angathandize ndani?

Mwati Elisa? Ndichoncho! Anakwera bulu n'kuthamanga kwambiri kuti akamupeze. Elisa anafika kunyumba kwake, nakwera yekha m'chipinda cham'mwamba, napemphera kwa Yehova. Mulungu anaukitsa mnyamatayo. Elisa anaitana mkazi nati, Nyamula mwana wako.



Iye ayenera kuti anasangalala kwambiri.

M'dziko lapafupi la Siriya munali mkulu wa asilikali dzina lake Namani. Iye anali wolimba mtima komanso wamphamvu, koma anali ndi nthenda yoopsa yakhate.

Mkazi wa Namani anali ndi kapolo wamng'ono amene anagwidwa ku Isiraeli. Mtsikana'yu anati: "Namani akanakhala ndi mneneri amene ali ku Isiraeli!"

Nthawi yomweyo Namani anapita kwa mneneriyo. Anatenga siliva, golide, ndi zovala zokongola monga mphatso.



Mtumiki wa Elisa anaturuka nati,

"Pita ukasambe kasanu ndi kawiri m'mtsinje wa Yorodano, ndipo udzakhala woyela. Namani anakwiya kwambiri. Kodi iye sakanakhoza kusamba mu mitsinje yoyera, yatsopano ya dziko lake lomwe, Syria? Mokwiya, anatembenuka n'kubwerera kwawo.

Mwamwayi Namani, atumiki ake anamuuza kuti amvere lamulo la Elisa. Chotero Namani anatsika naviika mu mtsinje wa Yorodano kasanu ndi kawiri. Ndipo Namani wakhateyo anachiritsidwa! Kenako Namani analambira Mulungu woona, Mulungu wa Elisa, Yehova amene anamuchiritsa khate.

Mulungu anagwiritsa ntchito mtumiki wake Elisa ngakhale atamwalira. Tsiku lina, munthu wina anaikidwa m'phanga limene Elisa anaikidwa kale. Mtembo wa munthuyo utakhudza mafupa a mneneriyo, munthuyo anatsitsimuka n'kuimirira. Ndithudi, Mulungu anasonyeza mphamvu Zake zazikulu kupyolera mwa mtumiki wake wokhulupirika, Elisa.

Elisa, Munthu Wozizwitsa

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

2 Mafumu 2-13

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16